The Malawi Government

# Ndondomeko ya Zachuma ya Mchaka cha 2025/2026 Mwachidule

**1**

## Chuma Cha Dziko la Malawi

Mchaka cha 2023, chuma cha dziko la Malawi chidakwera ndi 1.9 peresenti kusiyana ndi chaka cha 2022 pamene chidakwera ndi 0.9 peresenti. Izi zinali chomwechi chifukwa cha kuyenda bwino kwa ntchito za magetsi zomwe zinapangitsa kuti ntchito za mafakitale ziyende bwino. Ngakhale izi zinali chomwechi, Chumachi chinakhudzidwa ndi namodwe wa Freddy yemwe anasokoneza ntchito za ulimu. Kuwonjezera apo, chumachi chinakhudzidwaso ndi kuchepetsedwa kwa mphamvu kwa ndalama ya Malawi ndi 44 peresenti kulingana ndi ndalama ya kunja. Izi zinapangitsa kuti katundu akwere mitengo.

Mu chaka cha 2024, chuma cha dziko lino chinangokwera ndi 1.8 peresenti chifukwa cha nyengo yoyipa ya el nino. Koma mu chaka cha 2025, chuma cha dziko lino chikuyembekezereka kukwera ndi mulingo wa 3.2 peresenti chifukwa cha kugwa kwabwino kwa mvula komwe kukuyembekezereka kupangitsa kuti zokolola zikhale zochulukirako. Chumachi chikuyembekezekanso kukwera chifukwa cha ntchito zokopa alendo komaso za migodi.

Mitengo ya katundu idakwera kuchoka pa 28.8 peresenti mu 2023 kufika pa 32.2 peresenti mu 2024. Koma pali chiyembekezo choti mitengoyi idzitsika pang'onopang'ono kufika mpakana 24 peresenti mu 2025 chifukwa cha zokolola zochuluka zomwe dziko lino likuyembekezera kupeza komanso kukhazikika kwa mitengo ya mafuta agalimoto.

**2**

## Mmene Ndondomeko ya Chuma ya Mchaka cha 2025-26 Yakonzedwera

Ndondomeko ya zachuma ya mchaka cha 2025/26 yomwe ndi pafupiufupi K8 triliyoni, ndi yokulirapo ndi 28 peresenti kulekana ndi ndondomeko ya zachuma ya mchaka cha 2024/25 yomwe inali pafupifupi K6 triliyoni. Izi zili chomwechi kaamba koti boma likufuna kubweza ngongole zamgonagona zomwe lili nazo ku mayiko ndi mabungwe ongongoza ndalama, kufunikira kowonjezera ndalama ku ntchito zaumoyo, za maphunziro, komanso ntchito zina zokonzekera zisankho za panayi zomwe zidzachitike mchaka cha 2025.

### 2.1 Ndalama zonse zomwe Boma Lipeze mu 2025/26

Pali chiyembekezero choti mchaka cha chuma cha 2025-26, kuchuluka kwa ndalama zomwe boma litolere komanso kulandira kuchokera ku mayiko ndi mabungwe omwe amalithandiza dziko lino zifika pa K5.6 triliyoni (yomwe ndi 21 peresenti ya zachuma cha dziko). Mwa ndalamazi, K4.4 triliyoni ndi yomwe boma itolere mdziko mommuno komanso K1.1 triliyoni yochokera ku mayiko ndi mabungwe omwe amathandiza dziko lino pachuma.


Pa ndalama yolinganiziridwayi, pali chiyembekezo choti ndalama zotoleredwa ku misonkho zikwana K4.3 triliyoni yomwe ikuyimira 78 peresenti. Izi za wonjezereka ndi 45 peresenti kuyerekeza ndi zomwe zinapezeka mu 2024/25 zomwe zinali pafupi fupi K3 triliyoni; boma likuyembekezanso kutolera ndalama zokwana K106 biliyoni kuchokera ku mabugwe ndi nthambi za boma, yomwe ikuyimira 2 peresenti. Izi ndi zocheperako ndi 17 peresenti kulingana ndi zomwe boma linapeza mu chaka cha 2024/25 zomwe zinali K128 biliyoni; Boma likuyembekezeraso kuti mabungwe ndi mayiko omwe amalithandiza alipatsa ndalama zokwana K1.1 triliyoni, yomwe ikuyimira 20 peresenti ya ndalama zonse, izi ndi zotsika ndi 8 peresenti kulinganiza ndi K1.2 triliyoni ya mu chaka cha 2024/25.

Pa ndalama zokwana K1.1 triliyoni zomwe boma likuyembekezera kuti lirandira kuchokera ku mabungwe ndi mayiko omwe amalithandiza, K86.36 biliyoni idzachokera ku mayiko monga Norway, Germany ndi mayiko a UK pamene K1 triliyoni idzachokere ku mabungwe monga World Bank, African Development Bank, International Fund for Agricultural Development (IFAD), Flanders komanso Global Environmental Facility.

### 2.2 Mmene boma ligwiritsire ntchito ndalama

Mchaka cha zachuma cha 2025/26, boma likuyembekezera kugwiritsa ndalama zokwana pafupifupi K8 triliyoni (yomwe ili 31.1 peresenti ya chuma chomwe dziko lino limapeza (GDP)). Ndipo izi zikusonyeza kuti pali kukwera kwa 24.3 peresenti pa ndalama zomwe boma ligwiritse ntchito kulekana ndi K6.5 triliyoni yomwe idagwiritsidwa ntchito mu ndondomeko ya zachuma ya mchaka cha 2024/25. Pa ndalama imeneyi, K6 triliyoni igwiritsidwa pa ntchito za boma za tsiku ndi tsiku monga Kupereka chiwongola dzanja cha ngongole za boma, malipiro a anthu ogwira ntchito mboma, fetereza ndi mbeu zotsika mtengo, komaso kuyendetsa ntchito za boma.K2 triliyoni ndi ndalama yomwe igwire ntchito pa chitukuko cha dziko yomwe K578.51 biliyoni ya ndalama imeneyi ichokere ku misonkho yomwe boma litolere mdziko mommuno pamene mayiko ena atithandiza ndi ndalama yokwana K1.4 triliyoni.

CHINTHUNZI CHOYAMBA NDALAMA ZOTOLEREDWA 2025/26




**2.3 Kuchepa kwa ndalama yopita ku ndondomeko ya chuma ya boma**

Boma likuyembekezera kuti mchaka cha chuma cha 2025/26, ndalama zomwe layerekezera kuti ligwiritsa ntchito ziperewera ndi K2.5 triliyoni (yomwe ikuyimira 9.6 peresenti ya chuma chomwe dziko lino limapeza, GDP). Pali chilinganizo choti boma lidzabwereka ndalama ku mayiko akunja zokwana K145.78 biliyoni (zogwiritsa ntchito pa ntchito zachitukuko)) komanso ndalama zokwana K2.4 triliyoni zidzabwerekedwa m'dziko mommuno.

MOMWE NDONDOMEKO YA ZA CHUMA YAKONZEDWERA (MK' MA MILIYONI)

| Gawo | Zomwe zinavomerezedwa mu 2024/25 | Zowunikiridwaso mu 2024/25 | Zovemerezedwa mu 2025/26 |
|---|---|---|---|
| **Ndalama Zonse** | **4,552,220** | **4,354,520** | **5,578,445** |
| **Za Mdziko Mommuno** | **3,383,808** | **3,114,131** | **4,435,706** |
| Za Misonkho | 3,257,273 | 2,985,992 | 4,329,689 |
| Ziphaso ndi zina | 126,535 | 128,139 | 106,018 |
| **Chithandizo** | **1,168,412** | **1,240,389** | **1,142,739** |
| Kuchokera Ku mayiko akunja | 72,693 | 72,693 | 86,359 |
| Kuchokera ku mabugwe akunja | 1,095,719 | 1,167,696 | 1,056,379 |
| **Ndalama Zogwilira Ntchito** | **5,998,834** | **6,499,498** | **8,076,668** |
| **Zogwilira ntchito tsiku ndi tsiku** | **4,227,175** | **4,743,243** | **6,060,516** |
| **Zoperekedwa kwa ogwira ntchito mboma** | **1,121,981** | **1,326,526** | **1,588,824** |
| Malipiro | 1,075,232 | 1,288,179 | 1,532,258 |
| Zosonkha boma ku za opuma pa ntchito | 46,749 | 38,347 | 56,566 |
| **Chiwongola dzanja** | **1,455,690** | **1,424,678** | **2,171,506** |
| Cha ngongole za kunja | 79,750 | 82,153 | 61,176 |
| Cha ngongole za momuno | 1,375,940 | 1,342,525 | 2,110,330 |
| **Zolipilira katundu ndi ntchito** | **845,543** | **1,050,537** | **1,377,253** |
| **Chithandizo ku ma bungwe ena a boma** | **412,373** | **379,008** | **546,915** |
| Bungwe la Road Fund Administration | 85,024 | 69,056 | 101,122 |
| Bungwe la Roads Authority | 6,200 | 6,200 | 8,000 |
| Zopita ku MRA | 97,653 | 89,471 | 129,692 |
| Zopita kumabugwe aboma omwe amalandira zithandizo ku boma | 199,496 | 190,127 | 272,101 |
| Ngongole za ophunzira aku yuniversite | 24,000 | 24,000 | 36,000 |
| **Zothandizira anthu** | **358,613** | **378,055** | **286,282** |
| Zipangizo za ulimi zotsika mtengo | 161,285 | 131,585 | 111,450 |
| Fotereza otsika mtengo | 150,700 | 121,000 | 102,000 |
| Mbeu yotsika mtengo | 4,000 | 4,000 | 4,000 |
| Ziweto | 585 | 585 | 450 |
| Zogwiritsira ntchiro | 6,000 | 6,000 | 5,000 |
| Zopindulira omwe anapuma pa ntchito | 193,169 | 242,311 | 170,418 |
| Mtukula Pa khomo | 4,159 | 4,159 | 4,415 |
| **Zoperekedwa kwina** | **32,975** | **184,438** | **89,736** |
| **Zonse zopangira ntchito za chitukuko** | **1,771,658** | **1,756,255** | **2,016,152** |
| Za Chitukuko zo chokura kunja (Part I) | 1,387,058 | 1,310,239 | 1,437,639 |
| Za Chitukuko Zochokera mdziko mommmuno (Part II) | 384,600 | 446,016 | 578,513 |
| **Zonse zobwereketsa ndi kubwereka (net lending/borrowing)** | **-1,446,614** | **-2,144,978** | **-2,498,223** |

## 3

## Mmene boma lagawira ndalama ku nthambi zake

**3.1 Ndalama zolipira anthu ogwira ntchito mboma**

Boma mu chaka cha 2025/26 likuyembekezera kugwiritsa ntchito ndalama zokwana K1.5 triliyoni kulipira anthu ogwira ntchito mboma. Ndalamazi zakwera ndi 20 peresenti kuchoka pa K1.3 triliyoni ya mu chaka cha 2024/25. Ndalamazi zakwera chifukwa cha kukweza kwa malipiro komaso kulemba anthu ntchito.


**3.2 Ndalama za chipukuta misozi cha anthu opuma ntchito mboma**

Boma mu chaka cha 2025/26 layika padera ndalama zokwana K56 biliyoni za Chipukuta misozi kwa opuma kugwira ntchi mboma. Izi za kwera kuchoka pa K46 biliyoni ya muchaka cha 2024/25.

**3.3 Ndalama Zogwiritsa Ntchito tsiku ndi tsiku**

Boma lili ndi chiyembekezo choti mu chaka cha 2025/26 ligwiritsa ntchito ndalama zokwana K4.5 triliyoni, zomwe ndi zokwera ndi 42 peresenti kusiyana ndi zomwe zinavomerezedwa mchaka cha zachuma cha 2024/25. Ndipo ndalamazi zagawidwa motere: Kugula katundu ndi zina (K1.4 triliyoni); kubweza ngongole (K2.2 triliyoni); ndalama zopita ku nthambi zina zaboma (K547 biliyoni); zopita kwa opuma pa ntchito (K1.5 triliyoni).

CHITHUNZI CHACHIWIRI NDALAMA ZOGWIRITSA NTCHITO TSIKU NDI TSIKU




## 4


## Mmene ndalama zagawidwa mogwirizana ndi mfundo za chitukuko za Malawi 2063

Chomwe tajambula munsimu chikufotokoza momwe boma lagawira ndalama mogwirizana ndi ngodya za chitukuko komanso zothandizira kuti masomphenya omwe ali mu ndondomeko ya zachuma ya chaka cha 2063 atheke.

**Ngodya Za Chitukuko**

Monga mmene ziliri mu chithunzi chili pansipa, ndalama pafupi fupi K3.6 triliyoni zayikidwa ku ntchito zowonetsetsa kuti pali kayendetsedwe koyenera ka ntchito za boma (effective governance systems), ndalama zoposa K2.4 triliyoni zayikidwa ku ntchito zotukula ma luso (human capital development), komaso ndalama zosachepera K700 biliyoni zaperekedwa ku ntchito za ulimi.

CHITHUNZI CHACHITATU KAGAWIDWE KA NDALAMA MOLINGANA NDI NGODYA ZA MASOMPHENYA A 2063





## 5

## Ndalama zopita ku zigawo za ntchito za boma (sectors)

**Kagawidwe ka ndalama ku zigawo za boma**

Mu chithunzi chili pa mwambachi, mwazina, 34 peresenti ya ndondomeko ya za chuma yapita ku ntchito za kandetsedwe ka za chuma, 17 peresenti yapita ku ntchito za maphunziro, 10 peresenti yapita ku zitukuko za ulimi, 9 peresenti yapita ku ntchito za umoyo, 7 peresenti yapita ku ntchito za chitetezo.

CHINTHUNZI CHA CHINAYI KAGAWIDWE KA NDALAMA KU ZIGAWO ZA BOMA



## Ndalama zomwe zipindulire a Malawi (MK Mabiliyoni)




### Maphunziro ndi Ntchito Zaluso

| | |
|---|---|
| Sukulu za ukachenjede (yunivesite) | MK 150BN |
| Pulayimale, Sekondale ndi Zida Zophunzirira | MK 43BN |
| Ngongole za Ophunzira aku University | MK 36BN |
| Ntchito za omwe angomaliza kumene maphunziro | MK 3.7BN |

### Za Umoyo

| | |
|---|---|
| Pogula mankhwala | MK 78.7BN |
| Poyendetsa zipatala zazikulu | MK 54.4BN |
| Yokonzera zipatala za pa boma zomwe zawonongeka | MK 18BN |
| Pomanga zipatala | MK 4.5BN |
| Yogulira ma ambulance | MK 1.6BN |



### Ntchito Zamtengatenga ndi Mtokoma

| | |
|---|---|
| Pokonza misewu yatsopano | MK 160BN |
| Zokonzera misu yomwe yawonongeka | MK 10BN |
| Zotukula maulendo a pa ndege | MK 1BN |
| Yokonera doko la Likoma | MK 2BN |
| Zotukula maulendo a sitima za pamtunda (Njanji) | MK 2.5BN |

### Zotukula Miyoyo ya Anthu

| | |
|---|---|
| Ntchito za MoGCDSW m'maboma ang'ono ang'ono | MK 10.3BN |
| Ntchito za mtukula pakhomo | MK 4.4BN |
| Ndondomeko ya Dziko ya Ualbino ndi Thumbi la Ulemavu | MK 0.5BN |

### Ulimi, Ulimi Wamthirira, komanso Chitukuko cha Madzi

| | |
|---|---|
| Madzi ndi ukhondo | MK 279BN |
| Ntchito zogulira zipangizo za ulimi zotsika mtengo* | MK 112BN |
| Ntchito za ulimi wa mthilira | MK 123BN |
| Yaperekedwa kugulira chimanga choyika mu nkhokwe za boma | MK 60BN |
| Mega Farms | MK 38.3BN |

*

| | |
|---|---|
| Yogululira fetereza | MK 102BN |
| Yogulira mbeu | MK 4BN |
| Yonyamulira katunduyu | MK 5.5BN |





### Chitukuko Chakumudzi

| | |
|---|---|
| Anthu akumidzi kukhala odziimira paokha | MK 222BN |
| Ntchito ya chitukuko cha mmaboma ya GSED | MK 43BN |
| Thumba la chitukuko cha m'madera (CDF) | MK 42.4BN |
| Pomanga misewu ya mmizinda | MK 35BN |
| Chitukuko chomwe chimapezeka pa khonsolo (DDF) | MK 7.8BN |
| Miseu ya kumidzi | MK 2.5BN |
| Chitukuko cha madzi, monga kubowola | MK 2.3BN |



**Mlembi wamkulu wa mu unduna wa za chuma**
Imbani: +265 1 789 355
Imelo: budget@finance.gov.mw
www.finance.gov.mw